Kodi ndani anali ndi mphamvu yoposa ziŵanda ndipo nazitulutsa kunja?

_______________________

================================================================

7. Yesu anali ndi mphamvu yoposa ziŵanda. Popeza ife ndife ake a Yesu sitiyenera kukhala ndi mantha ndi ziŵandazo. Ziwanda zili ndi mphamvu. Koma Yesu ali ndi mphamvu yoposa. Ziwanda zimabweretsa mantha. Yesu amachotsa mantha ameneŵa. Yesu ali ndi mphamvu yoposa ziwanda. Yesu ali ndi mphamvu kuposa Satana mwini. Ife tikhoza kukhulupirira Yesu kuti atimasule kuchokera ku mantha ameneŵa.

Kodi munaonako anthu ali kuvutika ndi ziwanda? _______________

Kodi mumachita mantha ndi ziwandazo? _______________________

================================================================

8. Popanda mphamvu ya Yesu timachita mantha. Munthu amene anali m'sunagoge anali ndi chiŵanda chodetsedwa. Kodi pali ziŵanda zina zosadetsedwa? Ayi! Zonse ndi zoipa. Ziŵanda zimatumikira Satana. Nthaŵi zina anthu amene sakhulupirira mwa Yesu amaganiza kuti iwo ndi abwino. Koma ziŵandatu zimafuna kumangovutitsa anthu. Ziŵanda zimadziŵa kuti mdima unakonzedwera iwo. Ndipo zimafuna kuti anthu apite nawo kumeneko. Koma zimaopa Yesu.

1 Yohane 3:8:

Kukachita ichi mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge ntchito za m'direkezi.

Yakobo 2:19b

Ziŵanda zikhulupiriranso, ndipo zinthunthumira.

Kodi Yesu anachita chiyani kwa ziŵanda zomwe zimatidziŵitsa kuti Iye ali ndi mphamvu pa izo?

_______________________________________

================================================================

9. Yesu anatulutsa ziŵanda mwa anthu. Iye anatulutsa chiŵanda mwa **munthu wa m'sunagoge. Nthaŵi** ya madzulo a tsiku lomwelo, odwala ambiri

anadza kwa Yesu naŵachiritsa iwo.

Luka 4:41:

> Ndi ziŵanda zomwe zinatuluka mwa ambiri, ndi kufuula, kuti, "Inu ndinu mwana wa Mulungu." Ndipo Iye anazidzudzula, wosazilola kulankhula, chifukwa zinam'dziŵa kuti Iye ndiye Khristu.

Kodi timadziŵa bwanji kuti Yesu ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda?

________________________________________________________________

==========================================================================

10. Timadziŵa zimenezi chifukwa Yesu anazitulutsa mwa anthu. Yesu anabweretsa mbiri yabwino. Iye anabwera kudzamasula anthu kuchokera ku mphamvu za Satana. Iye anabwera kudzaŵamasula kuchokera kwa ziŵanda. Iye amachita zimenezi masiku ano.

Machitidwe 10:38:

> Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anam'dzoza Iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu;...amene anapitapita nachita zabwino, nachiritsa onse osautsidwa ndi m'dierekezi.

Pamene ife tili kuchita mantha ndi ziŵanda, kodi tiyenera kukhulupirira yani kuti atimasule ife?

________________________________________

==========================================================================

11. Tiyenera kukhulupirira Khristu.

1 Yohane 4:4:

> Inu ndinu ochokera mwa Mulungu, tiana, ndipo munailaka; pakuti Iye wakukhala mwa inu aposa iye wakukhala m'dziko lapansi.

Kodi ndimeyi ikulankhula za yani? Ikulankhula za Khristu ali mwa ife ndi Satana m'dziko lapansi. Ngati talandira Khristu sitiyenera kuchita mantha ndi Satana kapena amithenga ake. Sitiyenera kuchita mantha ndi zomwe ziŵanda zingatichitire. Ife tikhoza kukhulupirira Khristu kuti atimasule.

Ziŵanda zili za mphamvu koposa inu. Kodi ziŵanda ziri ndi mphamvu kuposa Yesu?

____________________________________

Kodi ife timadziŵa chiyani chomwe chimatithandiza kukhulupirira Khristu kuti akhoza kutimasula ku mantha woopa ziŵanda?

____________________

==========================================================

12. Ife timadziŵa kuti Khristu ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda. Pamene Yesu anatumiza ophunzira ake kukalalikira, Iye anaŵapatsanso mphamvu yoposa ziŵanda.

Luka 10:17:

> Ndipo makumi asanu ndi aŵiri aja anabwera mokondwera, nanena, Ambuye, zingakhale ziŵanda zinatigonjera ife m'dzina lanu.

Kodi kudziŵa kuti Yesu ali ndi mphamvu kuposa ziŵanda kumatithandiza kukhulupirira kuti achita chiyani?

______________________________

==========================================================

13. Kudziŵa zimenezi kumatithandiza kukhulupirira Khristu kuti atimasule kuchokera ku mantha a ziŵanda. Iye adzatisunga mwaufulu. Iye adzamasulanso anthu amene tikuŵathandiza. Iye anauza ophunzira kuti agwire ntchito yake.

Yohane 14:12,13:

> Indetu, indetu, ndinena kwa inu, wokhulupirira Ine, ntchito zimene ndichita Ine adzachitanso iyeyu; ndipo adzachita zoposa izi, chifukwa ndipita Ine kwa Atate. Ndipo chimene chilichonse mukafunse m'dzina langa, ndidzachichita, kuti Atate akalemekezedwe mwa Mwana.

Kodi ife timadziŵa bwanji kuti Yesu ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda?

__________________________________________

==========================================================

14. Yesu anatulutsa ziŵanda mwa anthu.

15. Zimatithandiza ife kukhulupirira Khristu kuti atimasule ife ku mantha woopa ziŵanda. Iye adzatimasula ife. Iye adzamasula abwenzi ndi anansi athu.

kodi masiku ano mumadziŵa wina wake yemwe ali ndi ziŵanda? __________

Kodi mukhoza kumupempherera kuti Khristu amupatse iye ufulu? __________

==============================================================

17. Tidzakambirana za zimenezi tonse pamodzi.

Kodi ife timadziŵa bwanji kuti Yesu ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda?

____________________________________________________________

Kodi kudziŵa zimenezi kumatithandiza kukhulupirira Yesu kuchita chiyani?

____________________________________________________________

==============================================================

SABATA LACHISANU: KHRISTU ATHANDIZA ANTHU
TSIKU LACHIŴIRI: YESU AONETSA KUTI IYE AMASAMALIRA ANTHU

1. Yesu anali ndi zinthu zambiri zoyenera kuchita pamene anali padziko lino lapansi. Iye anaonetsa zinthu zambiri. Dzulo tinaphunzira za ziŵanda.

Kodi timadziŵa bwanji kuti Yesu ali ndi mphamvu kuposa ziŵanda?

______________________________________________

Kodi kudziŵa zimenezi kumatithandiza ife kukhulupirira Yesu kuti angachite chiyani?

______________________________________________

==========================================================================

2. Ife timadziŵa kuti Yesu ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda chifukwa Iye anazitulutsa mwa anthu. Ngati titadziŵa zimenezi tikhoza kukhulupirira Khristu kuti atimasule ku mantha woopa ziŵanda.

Lero tiphunzira zozizwitsa zitatu zina za Yesu. Zozizwitsa zimenezi zimaonetsa kuti Yesu amasamalira anthu. Iye amasamalira mabanja athu, ntchito ndi moyo wathu.

(1) Yesu anasonyeza chisamaliro cha pa mabanja athu pochiritsa mpongozi wa Petro.
(2) Iye anasonyeza kuti amasamalira ntchito yathu pothandiza Petro kuti agwire nsomba zambiri.
(3) Iye anasonyeza kuti amasamalira miyoyo yathu pochiritsa munthu wa khate.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 5:1 mpaka 11. Kodi Yesu anasamalira zakuti Petro ndi abwenzi ake sanagwire kanthu usiku wonse?

______________________________________________

==========================================================================

3. Inde, Yesu amasamalira zinthu zimene zimationekera Kumbukirani kuti Yesu anali ku Kapernao. Iye anapita ku sunagoge. Kumeneko Iye anatulutsa chiŵanda mwa munthu. Ndipo Yesu anàpita ku nyumba ya Petro.

Luka 4:38-39:
Koma momwemo munali mpongozi wake wa Simoni, anagwidwa

ndi nthenda yolimba ya malungo; ndipo anapempha Yesu za iye.

Banja la Petro linadziŵa kuti Yesu amasamalira za anthu. Kodi mukuganiza kuti anafunsa kuti am'chitire chiyani mpongozi wake?

4. Iye anayenera kupempha Yesu kuti amuchiritse. Yesu anasamalira za mpongozi wake wa Petro.

Luka 4:39:

> Ndipo Iye anaimirira, naweramira pa iye, nadzudzula nthendayo; ndipo inamleka iye: ndipo anauka msangatu, nawatumikira.

Pamene munthu wachira kunthenda ya malungo nthaŵi zonse amakhala wofooka kwambiri. Pamakhala patapita masiku ambiri asakutha kugwira ntchito. Koma pamene Yesu anachiza mpingozi ameneyu anaimirira ndi kutumikira nthaŵi yomweyo. Imeneyi ndi njira imene anaonetsa kuthokoza kwake. Komanso iye anaonetsa mphamvu ya machiritso a Yesu.

Pambali poonetsa kuti Yesu akanakhoza kuchiritsa, kodi chozizwitsa chimenechi chinaonetsa chiyani za mphamvu ya Yesu?

5. Chinaonetsa kuti Yesu amatisamalira. Iye amasamalira za mabanja athu. Linali tsiku la sabata. Yesu anali kuphunzitsa m'sunagoge. Sunagoge anali malo amene Ayuda anali kukumanako kupembedza Mulungu. Aŵa anali malo omwe Mawu a Mulungu anali kuphunzitsidwako. Tsiku la Sabata ndilo linali lopuma Ayuda ndi kupembedza. Sabata ino tikhala tikuona kuti Ayuda sanafune Yesu kuti azichiza anthu pa tsiku la Sabata. Koma Yesu anasamalira za banja la Petro.

Kodi Yesu anachiza ndani wake wa Petro pa tsiku la sabata?

6. Iye anachiritsa mpongozi wa Petro. Yesu sanali kudera nkhaŵa za ophunzira ake okha. Iye anasamala ngakhale mabanja awonso. Madzulo amenewo pamene dzuŵa linali kuloŵa, anthu anali kubweretsa anthu a m'mabanja mwawo amene anali kudwala. Iwo anaŵabweretsa kwa Yesu.

Luka 4:40:
Ndipo pakuloŵa dzuŵa onse amene anali odwala ndi nthenda za mitundumitundu, anadza nawo kwa Iye;
Ndipo Iye anaika manja ake pa munthu aliyense wa iwo, naŵachiritsa.

Yesu atangotuluka m'sunagoge anachita zinthu zitatu zozizwitsa zomwe zinaonetsa kuti Iye amatisamalira.

(1) Kodi ndi chozizwitsa chiti chimene chinaonetsa kuti Iye amasamalira mabanja athu?

_______________________________________________

(2) Iye anaonetsa chisamaliro chake kwa ife pothandiza Petro kuti agwire nsomba zambiri.

(3) Iye anaonetsa chisamaliro cha miyoyo yathu pochiza munthu wakhate.

===========================================================================

7. Yesu anaonetsa kuti amasamalira mabanja athu pochiza mpongozi wa Petro. Simoni Petro anali msodzi wa nsomba. Iye anali ndi bwato la nsomba. Anthu anali kumutsatira Yesu kwambiri kuti amumve ali kuphunzitsa. Chifukwa cha ichi Yesu anakhala pansi m'bwato la Petro nayamba kuphunzitsa. Ndipo anauza Petro kuti asendeze bwato lake patali pang'ono pa kuya m'nyanja

Luka 5:45:
Ndipo pamene Iye analeka kulankhula, anati kwa Simoni, kankhira kwa kuya, nimuponye makoka anu kukasodza.
Ndipo Simoni anayankha, nati, "Ambuye tinagwiritsa ntchito usiku wonse osakola kanthu.

M'ndime imeneyi, kodi ndani anasonyeza kuti anasamalira za ntchito yathu?

_______________________________________________

===========================================================================

8. Yesu ndiye anaonetsa zimenezi. Iye anaonetsa kuti amasamalira za ntchito yathu. Petro anakhulupirira Yesu. Iye anamvera zomwe Yesu

ananena. Taonani zimene zinaoneka.

Luka 5:5-6:
"Ambuye, tinagwiritsa ntchito usiku wonse osakola kanthu! koma pa mawu anu ndidzaponya makoka." Ndipo pamene anachita ichi, anazinga unyinji waukulu wa nsomba; ndipo makoka awo anali nkung'ambika; ndipo anakodola anzawo a m'ngalawa inayo, adze aŵathangate, ndipo anadza, nadzaza ngalawa zonse ziŵiri.

Kodi ndi chifukwa chiyani ophunzira anagwira nsomba zambiri?

______________________________________________________________

========================================================================

9. Chinali chifukwa chakuti Yesu anaŵathandiza. Ophunzirawo anamvera zimene Yesu ananena. Pamene Petro anaona nsomba zonsezo, iye anagwada pansi pamaso pa Yesu. Yesu anamuuza kuti achoke. Koma Yesu anadziŵa mtima wa Petro. Iye anadziŵa kuti Petro sanafune kuti achokedi. Yesu anadziŵa kuti Petro anali kuchita mantha.

Luka 5:10:
Ndipo Yesu anati kwa Simoni, "Usaope kuyambira tsopano udzakhala nsodzi wa anthu.

Yesu anakonda Petro ndipo Iye anasamalira za ntchito yake. Kodi Yesu anaonetsa motani zimenezi? ________________________________________

________________________

========================================================================

10. Yesu anaonetsa zimenezi pothandiza Petro kuti agwire nsomba zambiri. Chimenechi chinali chozizwitsa chachikulu. Chimenechi chinathandiza Petro, Andreya, Yakobo ndi Yohane kukhulupirira mwa Yesu.

Luka 5:9-10:
Pakuti chizizwo chidagwira iye (Petro) ndi onse amene anali naye, pakusodzako kwa nsomba zimene anazikola; ndipo chimodzimodzinso Yakobo ndi Yohane ana a Zebedayo, amene anali anzake a Simoni.

Pamene Yesu anathandiza Petro kuti agwire nsomba zambiri, kodi chimenechi chinaonetsa chiyani za Yesu?

__________________________________________

__________________________________________________________________________

===========================================================================

11. Chinaonetsa kuti Yesu amasamalira za ntchito yathu.

Yesu ku Kapernao atangotuluka m'sunagoge anachita zozizwitsa zitatu zimene zinaonetsa kuti Iye amatisamalira.

(1) Iye anasonyeza chisamaliro chake cha mabanja athu pochiza mpongozi wa Petro.
(2) Kodi Iye anaonetsa kuti amasamalira za ntchito yathu motani?

______________________________________________________________

(3) Iye anaonetsa chisamalira cha miyoyo yathu pochiza munthu wa khate.

===========================================================================

12. Iye anasonyeza kuti amasamalira za ntchito yathu pothandiza Petro kuti agwire nsomba zambiri. Yesu sanali kuthandiza abwenzi ake okha. Iye anali kuthandizanso alendo. Mu mzinda umodzi Iye anapeza munthu wakhate. M'nthaŵi ya Yesu, anthu akhate anali kuchotsedwa. Iwo anali kuchotsedwa pakati pa anthu ena. Pamene anthu anali kudza pafupi nawo moŵayandikira anali kufuula mawu akuti, "wodetsedwa, wodetsedwa!" Aliyense anali kuthaŵa munthu wakhate.

Luka 5:12-13:

> Ndipo panali pamene Iye anali m'mudzi wina, taonani, munthu wodzala ndi khate; ndipo pamene anaona Yesu anagwa nkhope yake pansi nampempha Iye nanena, "Ambuye, ngati mufuna mungathe kundikonza." Ndipo Iye anatambalitsa dzanja lake, namkhudza, nanena, "ndifuna, takonzeka."

Kodi ndi munthu wotani amene anali kudedwa ndi anthu onse yemwe anakondedwa ndi Yesu?

______________________________________________________

===========================================================================

13. Ameneyu anali munthu wakhate. Yesu anamkonda iye. Iye anasamalira za moyo wake. Taonaninso zimene Yesu anachita.

Luka 5:13:

Ndipo Iye anatambalitsa dzanja lake, nam'khudza, nanena, "ndifuna, takonzeka." Ndipo pomwepo khate linachoka kwa iye.

Kodi ndi chozizwitsa chotani chimene Yesu anachitira moyo wa munthu ameneyu?

______________________________

==========================================================================

14. Yesu anamuchiritsa iye. Yesu anauza munthuyo kuti asauze aliyense koma apite kwa ansembe akadzionetse. Ndipo iye anayenera kupereka mtulo wa chopereka kwa ansembe. Chimenechi chidakaonetsa kuti iye alibwino. Chidakaonetsanso kuthokoza kwake kwa Mulungu. Yesu atangotha zimenezi anapita ku chipululu kukapemphera.

Pamene Yesu anachiritsa munthu wakhate, kodi iye anaonetsa kuti anasamalira za chiyani?

______________________________

==========================================================================

15. Chinaonetsa kuti Iye amasamalira za moyo wathu.

Yesu atatuluka msunagoge anachita zozizwitsa zitatu zimene zinaonetsa kuti Iye amatisamalira.

(1) Iye anaonetsa chisamalira chake cha pa mabanja athu pochiritsa mpongozi wa Petro.
(2) Iye anaonetsa chisamaliro cha ntchito yathu pothandiza ophunzira kuti agwire nsomba zambiri.
(3) Kodi Iye anaonetsa motani za chisamaliro cha miyoyo yathu?

______________________________

==========================================================================

16. Yesu anaonetsa chisamaliro cha pa miyoyo yathu pochiritsa munthu wakhate. Yesu amasamalira kumbali iliyonse ya miyoyo yathu. Nthaŵi zina Iye amatichitira zozizwitsa. Ndipo nthaŵi zina Iye amalola kuti tiphunzire pokhala ndi zinthu zotisautsa m'miyoyo yathu. Ife tiyenera

kukhala oyamika Mulungu pa zilizonse zimene amatichitira. Mpongozi wa Petro anaonetsa kuthokoza kwake potumikira Yesu. Petro anaonetsa kuthokoza potsatira Yesu ndi kukhala nsodzi wa anthu. Munthu wakhate anaonetsa kuthokoza popereka chopereka kwa ansembe.

Tiyeni tizionetsa chithokozo chathu kwa Yesu pokhala ndi miyoyo yomkondweretsa Iye. Tsopano tengani nthaŵi yomuthokoza chifukwa chokusamalirani.

==================================================================

17. Yesu ku Kapernao atatuluka msunagoge anachita zozizwitsa zitatu zimene zinaonetsa kuti Iye amatisamalira.

(1) Kodi Iye anaonetsa motani kuti amasamalira mabanja athu?

______________________________________________

(2) Kodi Iye anaonetsa motani kuti amasamalira ntchito yathu?

______________________________________________

(3) Kodi Iye anaonetsa motani kuti amasamalira miyoyo yathu?

______________________________________________

==================================================================

SABATA LACHISANU: KHRISTU ATHANDIZA ANTHU
TSIKU LACHITATU: KHRISTU ALI NDI MPHAMVU YOKHULULUKIRA MACHIMO

1. Dzulo tinaona pa zozizwitsa zitatu za Yesu. Tinaona kuti amatisamalira ife.

(1) Kodi Iye anaonetsa bwanji kuti amasamalira mabanja athu?

______________________________

(2) Kodi Iye anaonetsa motani kuti amasamalira ntchito yathu?

______________________________

______________________________

(3) Kodi Iye anaonetsa motani kuti amasamalira miyoyo yathu?

______________________________

______________________________

=====================================================================

2. Yesu anaonetsa chisamaliro cha mabanja athu pochiza mpongozi wa Petro. Iye anaonetsa chisamaliro cha pa ntchito yathu pothandiza Petro kuti agwire nsomba zambiri. Iye anaonetsa chisamaliro chapa miyoyo yathu pochiritsa munthu wakhate.

Yesu anachita zinthu zodabwitsa zambiri. Anthu anali kudabwa ndi mawu a Yesu. Iye anali kulankhula ndi mphamvu. Anthu anadziŵa kuti ayenera kumumvera ndi kukhulupirira. Anthu anali kudabwanso ndi ntchito za Yesu. Iye anatulutsa ziŵanda. Anali kuchiza anthu odwala. Koma Yesu anachita chinthu chachikulu kuposa zonsezi. Iye anakhululukira machimo. Chimenechi ndi chimene tikhale tikuphunzira lero.

| |
|---|
| Pamene munthu wodwala anatsitsidwa kuchokera pa denga, Yesu anachita kanthu kena koposa kumuchiritsa. Iye anakhululukira machimo ake. |

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 5:17-26. Werenganinso ndime 18. Kodi ndi chiyani chinali chovuta kwa munthu ameneyu?

______________________________
=====================================================================

3. Munthu ameneyu anali wamanjenje. Izi zikutanthauza kuti iye sanali kutha kusuntha. Iye sanali kutha kuyenda. Sanali kutha kudzidyetsa yekha. Sanali kutha kukhala tsonga. Mwina iye sanali kutha ndi kulankhula komwe. Pano tikuonanso kuti Yesu ali kuchitanso chozizwitsa. Iye anachiritsa munthu amene anali ndi matenda woopsaŵa.

Kodi chinali chinthu chaching'ono kwa Yesu kuti achiritse munthu ameneyu?

---

==========================================================================

4. Chinali chinthu chachikulu kwa Yesu kuti achize munthu ameneyu. Yesu anali atachiza kale anthu ambiri. Koma munthu ameneyu anali m'mavuto a akulu kwambiri. Iye sakanakhoza kudza kwa Yesu yekha. Abwenzi ake anayi anamuthandiza. Iwo anapanga kama wamng'ono woti amunyamulire. Koma pamene iwo anafika kunyumba imene kunali Yesu sanakhoza kuloŵamo. Nkutheka kuti iwo anali okwiya kwambiri. Koma iwo anali ndi chikhulupiriro chachikulu. Iwo anaona kuti denga la nyumbayo linapangidwa ndi njerwa za phanthiphanthi.

Luka 5:19:
Chifukwa cha unyinji wa anthu, anakwera pamwamba pa tsindwi, namtsitsira iye poboola pa tsindwi ndi kama wake, namfikitsa pakati pomwe pamaso pa Yesu.

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi abwenzi anamulowetsa wodalayo mnyumba motani?

---

---

==========================================================================

5. Iwo anamulowetsa kupyolera pa denga. Choncho, unyinji wa anthu unadza tsopano kudzamva Yesu ali kulankhula. Ena mwa iwo anali Afalisi. Afalisi anali Ayuda omwe anali kutsata malamulo ambiri. Iwo anali ndi malamulo a Kapempheredwe, kasamalidwe, kaperekedwe ka ndalama. Iwo anali ndi malamulo akatsukidwe ka mbale zawo ndi kasambidwe ka matupi awo. Afalisi anaonjezera malamulo ambiri ku malamulo a Mose. Iwo anali kuonetsetsa ngati Yesu angaphwanye malamulo awo.

Luka 5:20:
Ndipo Iye, pakuona chikhulupiriro chawo cha anthu amene anabweretsa munthu wodwalayo) anati, "munthu iwe machimo ako akhululukidwa."

Werenganinso ndime izi kachiŵiri ndipo lembani zomwe Yesu ananena kwa munthu wodwalayo.

______________________________________________________

______________________________________________________

==========================================================================

6. Iye anati, "munthu iwe matchimo ako akhululukidwa." Chimenechi chinali chinthu chodabwitsa kunena chomwechi! Afalisi anakhala okwiya kwambiri. Iwo anali kuganiza kuti ali kuseka Mulungu. Iwo anaganiza kuti Iye anali Mulungu pochitira Mulungu mwano.

Luka 5:21:
Ndipo Alembi ndi Afalisi anayamba kuyesayesa mumtima mwawo, kuti, "ndani uyu alankhula zochitira Mulungu mwano? Ndani angathe kukhululukira machimo, koma Mulungu yekha?

Kodi ndani adakhoza kunena kuti, "machimo ako akhululukidwa" chifukwa iye anali Mulungu?

______________________________________________________

==========================================================================

7. Yesu adakhoza kuchita zimenezi. Koma Afalisi anakhala adani ake. Iwo anayamba kulankhula mawu oipa aukali pakati pawo onena zomwe wachita Yesu.

Luka 5:22-24:
Koma Yesu anadziŵa zoyesayesa zawo, nayankha, nati kwa iwo, Muyesayesa bwanji m'mitima yanu? Chapafupi nchiti, kunena, Akhululukidwa kwa iwe machimo ako; kapena kunena, Tauka, nuyende? Koma kuti mudziŵe kuti Mwana wa munthu ali nayo mphamvu pa dziko lapansi yakukhululukira machimo, (anati Iye kwa wamanjenjeyo ), Ndinena kwa iwe, Tauka, nusenze kama wako numuke kunyumba kwako.

Munthu wodwalayo anaimirira nayamba kuyenda. Kodi Yesu anali ndi mphamvu yokhululukira machimo?

______________________________________________________

==========================================================================

8. Inde, Yesu anali ndi mphamvu imeneyi. Iye anaionetsa kwa Afarisi pochiritsa munthu ameneyu. Yesu anati, "munthu iwe machimo ako akhululukidwa." Afarisi sanathe kuona ngati kanthu kena kanachitika mumtima mwake. Yesu anati, "Tauka nusenze kama wako, numuke kunyumba kwako." Pamenepo ndi pamene anaona kuti munthuyo wachiritsidwa. Yesu anagwiritsa ntchito kanthu kena komwe anakhoza kukaona kuti aonetse kanthu kena komwe sakadakaona.

Yesu akadakhoza kuchita kanthu kena kakakulu koposa kuchiza thupi la munthu. Kodi chinali chiyani? ______________________________

______________________________________________________________

===================================================================

9. Yesu akhoza kukhululukira machimo. Yesu anati akhoza kuchiritsa thupi la munthu. Chimenechi chinaonetsadi kuti Iye ali ndi mphamvu. Chinaonetsa kuti ali ndi mphamvu yakuchita zimene Iye anali kunena kuti akhoza kuchita. Chinaonetsa kuti Iye ali ndi mphamvu yokhululukira machimo.

Luka 5:25:

> Ndipo pomwepo anaimirira pamaso pawo, nasenza chimene adagonapo, nachokapo, kunka kunyumba kwake, wakulemekeza Mulungu.

Kodi ndi kupyolera mwa munthu uti amene Yesu anaonetsa kuti akhoza kukhululukira machimo?

______________________________________.

===================================================================

10. Zinali kupyolera mwa munthu wodwala. Zinali kupyolera mwa munthu amene anatsitsidwa kupyolera pa tsindwi la nyumba. Koma munthu aliyense amafunika kuti machimo ake akhululukidwe. Yesu anauza ophunzira ake kuti alalikire za zimenezi. Pamene Iye anali wokonzeka kubwerera kumwamba anati chiyenera kumalalikidwa kwa anthu onse. Ophunzira analalikira za zimenezi.

Luka 24:47:

> Ndi kuti kulalikidwe m'dzina lake kulapa ndi kukhululukidwa kwa machimo kwa mitundu yonse.

Machitidwe 10:34,43:

> Ndipo Petro anatsegula pakamwa pake nati, ...Ameneyu aneneri

amchitira umboni, kuti onse akumkhulupirira Iye adzalandira chikhululukiro cha machimo awo mwa dzina lake.

Kodi ndi ndani angakhululukire machimo ndikuti kutereku ndiko kuchita chinthu chachikulu kuposa kuchiritsa thupi la munthu?

___

================================================================

11. Ndi Yesu yekha angathe kuchita zimenezi.

Machitidwe 4:12:

Ndipo palibe chipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu limene tiyenera kupulumutsidwa nalo.

Aroma 3:23:

Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemelero wa Mulungu.

Mwina ife tiri ndi matupi olimba amene safunika kuchiritsidwa koma tonse tikusoŵa kanthu kena komwe Yesu yekha ndiye angakachite. Kodi ndi chiyani?

___

___

================================================================

12. Tonse timafunika kukhala okhululukidwa machimo athu. Tonse tinachimwa. Munthu nkutheka kukhala ndi thupi la mphamvu ndi kukhala osadwaladwala. Koma ngati iye ali ndi machimo ake sangathe kukhala wokondwa kwenikweni. Njira imeneyi ndi imene ophunzira anali kulalikira pamene Yesu atabwerera kunka kumwamba.

Machitidwe 13:38, 39:

Potero padziŵike ndi inu amuna abale, kuti mwa Iye chilalikidwa kwa inu chikhululukiro cha machimo; ndipo mwa Iye yense wokhulupira ayesedwa wolungama kumchotsera zonse zimene simungathe kudzichotsera poyesedwa wolungama ndi chilamulo cha Mose.

Kodi chinthu chabwino ndi chiti, kukhala ndi thupi la moyo wabwino tsopano kapena kukhala wokhululukidwa machimo kwa nthaŵi zonse?

___

13. Ndi kwabwino kukhala okhululukidwa. Ndipo tidzakhoza kupita ndi kukakhala ndi Mulungu. Ife sitidzalangidwa ndi imfa ndi kusiyanitsidwa ndi Mulungu.

Pamene munthu wodwala uja anatsitsidwa kuchokera pa mwamba pa tsindwi, kodi Yesu anachita chiyani chimene chinali cnachikulu kuposa kumuchiritsa Iye?

________________________________________________

==========================================================================

14. Yesu anakhululukira machimo ake. Anthu ena amakhala okaika ndi machimo ngati anakhululukidwa. Iwo amafunika kukhulupirira Mawu a Mulungu. Nazi ndime ziŵiri zimene zingakuthandizeni.

1 Yohane 1:9:

Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse.

Akolose 1:13-14:

Amene anatilanditsa ife ku ulamuliro wa mdima, natisunthitsa kutiloŵetsa m'ufumu wa Mwana wa chikondi chake; amene tiri nawo maomboledwe mwa Iye, m'kukhululukidwa kwa zochimwa zathu.

Kodi inu mumadziŵa bwanji kuti machimo anu anakhululukidwa?

________________________________________________________

==========================================================================

15. Tidzakambirana za ichi m'kalasi.

Pamene munthu wodwala uja anatsitsidwa kuchokera pamwamba pa tsindwi, kodi Yesu anachita chiyani chimene chinali chachikulu kuposa pomuchiritsa Iye?

________________________________________________

==========================================================================

SABATA LACHISANU: KHRISTU ATHANDIZA ANTHU
TSIKU LACHINAYI: IYE ANAPHUNZITSA ZA KUPEMBEDZA KOONA

1. Sabata ino tiphunzira mmene Yesu anathandizira anthu. Taphunzira kale chinthu chachikulu chimene Iye anachita.

Pamene munthu wodwala uja anatsitsidwa kuchokera pamwamba pa tsindwi, kodi Yesu anachita chiyani chimene chinali choposa kumuchiritsa?

__________________________________________________________

==========================================================

2. Yesu anakhululukira machimo komanso anamuchiritsa. Zimenezi zinakwiitsa Afarisi ndipo anakhala adani a Khristu chifukwa sanamvere malamulo awo. Iye sanagwirizane ndi njira za mapembedzedwe awo. Tiona mmene Afarisi anatsutsira Yesu. Tionanso Yesu mmene anaphunzitsira kapembedzedwe koona. Zimenezi ndi zimene tiphunzire lero.

(1) Afarisi anali gulu la Ayuda amene anayesetsa kusunga malamulo ambiri koma sanali kupembedza Mulungu moona.

(2) Tiyenera kupembedza Mulungu potsata Yohane 4:24. amene amati: Mulungu ndiye Mzimu; ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira muuzimu ndi m'choonadi.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 5:27-39. Kodi Afarisi anamvetsetsa zimene Yesu anali kuphunzitsa?

____________________

==========================================================

3. Iwo sanali kumvetsetsa. Dzulo tinaona kuti iwo anali kusamalitsa kwambiri za kapempheredwe, kusala ndi kasambidwe. Iwo anali kupereka ndalama zambiri kwa anthu osauka. Koma iwo anali onyada ndipo sanali kukonda anthuwo. Iwo anali kufuna kudzitumikira okha.

Kodi Afarisi anali kuganiza kuti akhoza kuchita chiyani ngati iwo asunga malamulo ambiri?

___________________________________________

===================================================

4. Iwo anali kuganiza kuti akhoza kudzipulumutsa okha. Iwo anali ndi malamulo ambiri amene anaonjezera ku malamulo a Mose. Iwo anadzipangira okha malamuloŵa. Yesu anauza mkazi waku Samariya kuti anthu azipembedza Mulungu muuzimu ndi m'choonadi. Yesu anadziŵa mitima ya anthu. Chifukwa cha ichi Iye sanasankhe omutsatira kuchokera kwa atsogoleri a Aisraeli. Mmodzi wa anthu amene Iye anasankha anali wokhumetsa msonkho. Mateyu anakhala wotsatira woona ndi wopembedza moonadi.

Kodi ndi anthu ati amene anasankha kudzipulumutsa okha posunga malamulo?

____________________________________________

==========================================================================

5. Afarisi anali kuyesa kudzipulumutsa okha. Iwo anali kusunga malamulo ambiri. Iwo anali kupembedza Mulungu m'njira yawoyawo. Koma Mateyu anatsatira Yesu.

Luka 5:27-28:

> Ndipo zitatha izi Iye anatuluka, naona munthu wamsonkho, nati kwa iye, "Unditsate Ine." Ndipo iye anasiya zonse, nanyamuka, namtsata Iye.

Mateyu anaphunzira kupembedza Mulungu moonadi. Patapita nthaŵi iye analemba buku loyamba la m'Chipangano Chatsopano lotchedwa Mateyu. Koma Afarisi anayesetsa kutenga njira yawoyawo. Iwo anadziŵa kuti Mulungu amaona zimene timachita. Iwo anaiŵala kuti, Mulungu amaona maganizo athunso. Iye amadziŵa chifukwa chimene ife timachitira zinthu. Iye amatizindikira bwino pa zimene timachita.

Kodi Afarisi anali kupembedza Mulungu moonadi? ____________________

==========================================================================

6. Iwo sanali kupembedza moonadi. Yesu atangotha kuitana Mateyu (kapena Levi); Mateyu anachitira Yesu phwando. Iye anaitana abwenzi ambiri kuti abwere. Ena mwa iwo anali okhometsa misonkho monga Mateyu. Koma Afarisi ena anabwera kudzangoona zochitikazo. Iwo sanali kumvetsetsa kuti Yesu anadza kudzapulumutsa ochimwa kuti azipembedza moonadi.

Kodi ndi gulu liti la anthu m'nthaŵi ya Yesu linayesa kusunga malamulo koma sanathe kupembedza Mulungu moonadi?

__________________________

7. Ameneŵa anali Afarisi. Afarisi anali kumunenera Yesu ndi ophunzira ake zinthu zoipa. Iwo anali kunena kuti sanali kusala kaŵirikaŵiri kapena kumapemphera pa nthaŵi zapadera. Afarisi anali kusala kuti anthu aziŵatama.

Kodi munthu ayenera kusala kuti azikondweretsa anthu? Ayi, Iye ayenera kusala kuti azikondweretsa Mulungu. M'Buku Lopatulika Mulungu sanasankhe masiku apadera amene ali woyenera kusala. Munthu ayenera kusala pokhapokha kanthuko kali kofunika koposa chakudya. Kupembedza koona kumatsata malamulo opangidwa ndi anthu.

Yohane 4:24:
Mulungu ndiye Mzimu; ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira muuzimu ndi m'choonadi.

Kodi ndani amaphunzitsa njira ya kupembedza Mulungu moonadi?

---

==========================================================================

8. Yesu anaphunzitsa njira ya kupembedza koonadi. Iye sanadze kudzapanga malamulo ena ambiri monga malamulo a Ayuda. Iye anati munthu saika chigamba chakale pa malaya atsopano. Yesu sanali kukonza njira zakale za anthu. Iye anali kusintha mitima ya anthu. Iye anali kufuna kupanga anthu atsopano kuchokera mwa iwo. Iye anafuna kuti anthu azipembedza Mulungu moonadi.

Luka 5:36:
Palibe munthu ang'amba chigamba cha malaya akale;
chifukwa ngati atero, angong'ambitsa atsopanowo,
ndi chigamba chatsopanocho sichidzayenerana ndi akalewo.

Kodi ndi gulu liti la Ayuda m'nthaŵi ya Yesu lomwe linayesa kusunga malamulo ambiri koma sanali kupembedza Mulungu moonadi?

---

==========================================================================

9. Iwo anali Afarisi. Koma Yesu anaphunzitsa njira ya kupembedza koona Iye poyamba anafotokozera mkazi waku Samariya. Iye anati tiyenera kupembedza muuzimu ndi m'choonadi. Kupembedza kumatanthauza kuonatsa ulemu waukulu kwa Mulungu. Kumatanthauza kuyamika Mulungu ndi kupemphera kwa Iye. Mulungu ndiye wamkulu koposa kulikonse. Iye ndiye mlengi wathu. Iye alibe thupi lofanana ndi lathu. Iye anatumiza mwana wake kudziko lapansi kudzakhala m'thupi kutionetsa ife chikondi chake.